# PHUNZIRO LA 67

1. M'munda wa Getsemane, Yesu anayamba kupenphera, Iye atakhumudwa ndikuvutika mu mtima kwambiri.
-Kodi chifukwa chiyani Yesu anakhumudwa ndikuvutika mu mtima?
-Chifukwa chakuti Iye anadziŵa kuti kuvutika kumene kunkadza kwa Iye, kunali kuvutika kowopsya kwambiri kumene wina aliyense sanakuwoneko.

2. Kodi amene ankalitsogolera khamu la anthu amene ananyamula malupanga ndi zibonga anali ndani?
-Yudasi.

3. Kodi amene ankamutsogolera Yudasi kukamugwira Yesu anali ndani?
-Satana.

4. Kodi ndi ndani wina amene amatsogoleledwa ndi Satana?
-Anthu onse amene amakana kumvera Mawu a Mulungu, nawonso amatsogoleledwa ndi Satana.

5. Kodi chifukwa chiyani ophunzira a Yesu onse anathaŵa?
-Ophunzira a Yesu ankawopa kwambiri ndiponso sankamvetsetse chifukwa chimene Yesu amagwidwira.

6. Kodi ophunzira a Yesu sankamvetsetsa chiyani?
-Ophunzira a Yesu sankamvetsetsa za m'mene Yesu angakhalile Mpulumutsi ngati Iye atagwidwa ndi kuphedwa.

7. Kodi anthu amene anamugwira Yesu anamutengera kuti?
-Anthu amene anamugwira Yesu aja anamutengera Iye

kwa wamkulu wa amsembe.

8. Kodi chifukwa chiyani atsogoleri a Ayuda sanamupeze Yesu ndi china chilichonse chochimwa?
-Chifukwa chakuti Yesu sanachite china chilichonse chochimwa.
-Chifukwa chakuti Yesu sanachite tchimo lina lililonse.

9. Kenako, mkulu wa amsembe uja atayankhula kwa Yesu ndikumufunsa Iye kuti ngati ali Kilisitu, Mwana wa Mulungu, kodi Yesu anayankha chiyani?
-Yesu anayankha kuti, "Ndine amene. Ndipo mudzamuwona Mwana wa Munthu atakhala ku dzanja la manja la Wanphamvu zonse, akudza ndi mitambo ya kumwamba. "

10. Kodi chifukwa chiyani mkulu wa amsembe uja analankhula kuti Yesu ayenera kuphedwa?
-Mkulu wa amsembe uja analankhula kuti Iye wanyoza Mulungu.

11. Kodi Yesu ananyoza Mulungu?
-Ayi.

-Akuluakulu a amsembe pamodzi ndi atsogoleri a Ayuda atatha kumulamula Yesu kuti aphedwe, anamutumizanso kwa Pilato.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:1

1-M'mamaŵa kwambiri, akuluakulu a amsembe, aphunzitsi a malamulo ndi akuluakulu a milandu onse, anakhala upo nagwirizana zom'manga Yesu, namtenga, nampereka kwa Pilato.



Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:42-46

42-Linali tsiku lokonzekera (ilo linali tsiku la pambuyo pa tsiku la sabata). Chomcho madzuro atafika,
43-Yosefe wa ku Arimateya, mkulu wa milandu, omveka, amene payekha anali kuyembekezera Ufumu wa Mulungu, anapita molimba mtima kwa Pilato kukapenpha mtembo wa Yesu
44-Ndipo Pilato anazizwa pakumva kuti Iye anali atamwalira kale. Kenako anamuyitana Kenturiyo, namufunsa ngati Yesu wamwaliradi.
45-Iye atamva kwa Kenturiyo kuti zinali chomwecho, analipereka thupi [la Yesu] kwa Yosefe.
46-Ndipo Yosefe anagula nsaru ya bafuta, namutsitsa Iye, namukurunga m'bafutamo, namuyika m'manda osemedwa m'thanthwe; nagudumuzira mwala pa khomo la mandalo.

-Yosefe wa ku Arimateya, anali munthu wa chuma amene ankakhulupilira kuti Yesu anali Mulungu Mpulumutsi.

-Yesu atamwalira, Yosefe anapita kwa Pilato ndipo anakamupenpha iye kuti akayike mtembo wa Yesu.

-Kenako, Yosefe anawutenga mtembo wa Yesu ndikukawuyika m'manda ache.

-Ngati m'mene Mulungu ananenera kudzera mwa aneneri mu zaka zambiri zapitazo, Yesu anayikidwadi m'manda ndi munthu wa chuma.

-Kodi amene anang'amba chinsarucho kuchokera pam-
wamba mpakana pansi anali ndani?
-Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anaching'amba chinsaru-
cho paŵiri?

-Mulungu anaching'amba chinsarucho paŵiri kuwonetsa kuti panalibenso kusiyana pakati pa munthu ndi Mulungu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:39

39-Ndipo Kenturiyo, amene anayimilira mo-
yang'anizana ndi Iye, anamva kulira kwache ndipo ana-
wona m'mene Iye anafera, chomcho iye anati kuti,
"Zowonadi Munthu uyu anali Mwana wa Mulungu!"

-Pamene Kunturiyo , amene anali wamkulu wa asilikali makumi khumi, anamuwona Yesu akumwalira, iye anad-
ziŵa kuti Yesu analidi Mulungu Mpulumutsi.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:40-41

40-Panalinso azimayi ena amene ankayang'anira
zimene zinkachitika chapatali. Mwa iwo anali Mariya wa
ku Magadala, Mariya amache a Yakobo wang'ono
ndiponso a Yose ndi Salome.
41-Ku Galileya, azimayi ameneŵa ankamutsata Iye
ndikumamutumikira. Azimayi enanso ambiri amene anad-
za naye pamodzi ku Yerusalemu, analinso pomwepo.

-Azimayi aŵa anali azimayi amene anakhulupilira mwa Mulungu, ndipo anadziŵa kuti Yesu anali Mulungu Mpulumutsi.



-Kodi Pilato anali ndani?
-Pilato anali mfumu ya ku Yuda amene anasankhidwa ndi Kayesara, mfumu ya Aloma.

-Kuti Ayuda amuphe Yesu, anayenera kulandira chilorezo kuchokera kwa Pilato.

-Yesu atamutengera pa maso pa Pilato, Pilato anamufun-
sa Iye funso.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:2

2-Ndipo Pilato anamufunsa Iye kuti, "Kodi ndi iwe
mfumu ya Ayuda?" Ndipo [Yesu] anayankha kuti,
"Mwatero ndi inu."

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anati kuti Iye ndi Mfumu ya Ayuda?
-Chifukwa chakuti Iye anali chidzukulu cha Davide.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:3-5

3-Ndipo akuluakulu a amsembe anamunenera zin-
thu zambiri Iye.
4-Ndipo Pilato anamufunsanso [Yesu] kuti, "Kodi
siwuyankha kanthu? Tawona zinthu zambiri zimene aku-
kunenera iwe."
5-Koma Yesu sanayankhenso kanthu, kotero kuti
Pilato anazizwa.

-Ngakhale kuti anthu ankamunenera Yesu zinthu zambiri zabodza, Iye anangokhala chete, osayankha china chili-
chonse.

-Ngati m'mene Mulungu analankhulira kudzera mwa ane-

neri mu zaka zambiri zapitazo, Mpulumutsi anakhaladi chete ataneneredwa zinthu zambiri zabodza.

-Pa nthaŵi ya phwando la Pasaka, unali mwambo wa Pilato oŵamasulira wandende m'modzi Ayuda.

-Chomcho, Pilato anaŵafunsa Ayuda ngati akufuna kuti aŵamasulire Yesu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:6-11

6-Ndipo unali mwambo wawo omasura wa ndende m'modzi amene anthu angamusankhe pa mphwando lawo.
7-Ndipo panali munthu wina wache dzina lache Baraba amene anali ndi amzache awupandu, amene anapha munthu mu upanduwo.
8-Ndipo khamu la anthu linabwera kudzamupenpha Pilato kuti aŵachitire iwo monga m'mene amaŵachitilira nthaŵi zonse.
9-Ndipo Pilato anafunsa kuti, "Kodi mukufuna kuti ndikumasulireni mfumu ya Ayuda?"
10-akudziŵa kuti akuluakulu a amsembe anamupereka Iye mwanjiru.
11-Koma akuluakulu a amsembe analisonkhezera khamulo kuti limuwuze Pilato kuti aŵamasulire Baraba m'malo mwache.

-Pilato anadziŵa kuti Yesu sanachite chochimwa chilichonse.

-Pilato anadziŵa kuti akuluakulu a Ayuda anamugwira Yesu chifukwa cha njiru.

-Chomcho, Pilato ankaganiza kuti Ayuda amusankha



-Kusiyana ndi Mulungu Atate ndi chilango chowopsya kwambiri pa dzilo la pansi pano.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:37

37-Ndi mawu okweza, Yesu anapuma mpweya wache omaliza.

-Yesu anamwalira pa mtanda paja.

-Kodi chinachitika nkachisi ndi chiyani Yesu atamwalira?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:38

38-Ndipo chinsaru chotchinga cha mkachisi chinang'ambika pakati, kuyambira pamwamba mpaka pansi.

-Kodi chinsaru chotchinga cha mkachisi chinali chiyani?
-Chinali chinsaru chimene chinkasiyanitsa Chipinda Choyera ndi Chipinda Choyeretsetsa kwambiri.

-Kodi chinsaru chotchingacho chinali chizindikiro cha chiyani?
-Chinali chizindikiro cha kusiyana pakati pa Mulungu ndi munthu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anasiyana ndi munthu?
-Chifukwa cha tchimo.

-Chifukwa cha tchimo lanthu, Mulungu ndi Munthu anasiyana, ndipo palibe amene ankatha kuloŵa M'chipinda Choyeretsetsa kwambiricho kupatula wankulu wa wa amsembe amene ankaloŵa kamodzi kokha pa chaka.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:35-36

35-Anthu amene anayima pafupi ndi Iye atamva izi anati kuti, “Tamvani, akuyita Eliya.”
36-Ndipo munthu wina anathamanga, nadzadza chinkhupule ndi vinyo osasa, nachiyika pa bango, namumwetsa Iye. Kenako anati kuti, “Tsopano musiyeni yekha. Tiyeni tiwone ngati Eliya abwere kudzamutsitsa Iye”

-Anthu amene ankamuwona Yesu akufa pa mtanda paja ankaganiza kuti Iye akumuyitana Eliya.

-Yesu sanali kuyitana Eliya.

-Yesu ankalilira kwa Mulungu Atate.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu ankalilira kwa Mulungu Atate?

-Chifukwa chakuti Mulungu Atate anamusiya Yesu, chimenecho chinali chilango chowopsya kwambiri.

-Kodi Yesu wakhala ali ndi Mulungu Atate kwa nthaŵi yayitari bwanji?.
-Nthaŵi zonse.

-Kodi panali nthaŵi imene Mulungu Atate ndi Yesu anasiyanako?
-Palibe.

-Chifukwa chakuti iyi inali nthaŵi yoyamba imene ili yokhayonso imene Mulungu Atate anasiyana ndi Yesu, Yesu analira.



Yesu kuti amasulidwe.

-Koma m’malo mwake, akuluakulu a amsembe analisonkhezera khamu la anthu lija kuti limukakamize Pilato kuti am’masule Baraba, wakupha, m’malo mwa Yesu.

-Kenako Pilato anaŵafunsa funso Ayuda.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:12-14

12-Kenako Pilato anaŵafunsanso kuti, “Kodi ndidzachite chiyani ndi Iye amene mukumutchula kuti ndi mfumu ya Ayuda?”
13-Anthu anafuwula kuti, “Mpachikeni!”
14-Pilato anafunsanso kuti, “Kodi chifukwa chiyani? Nanga wachita chiyani choyipa?”

-Ngakhale kuti Yesu sanachimwe china chilichonse, khamu la anthu lija linamuda Yesu ndipo linafuna kuti Iye apachikidwe basi.

-Ngati m’mene Mulungu ananenera kudzera mwa aneneri mu zaka zambiri zapitazo, Yesu anayeneradi kudedwa popanda chifukwa china chilichonse.

-Khamu la anthu linafuna kuti limupachike Yesu pa mtanda.

-Kodi kupachikidwa nd chiyani?
-Ndi kukhomera pa mtanda manja ndi mapazi a munthu, ndikumusiya pomwepo mpaka amwalire.

-Kupachikidwa ndi imfa yopweteka ndipo yowopsya kwambiri, imene Aloma amayigwiritsa ntchito polanga anthu olakwa kwambiri.

-Kenako Pilato analamula kuti Yesu akwapulidwe.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:15

15-Ndipo Pilato pofuna kuŵakhazika pansi mitima anthuwo, anaŵamasulira Baraba, nampereka Yesu kwa iwo atamukwapula kuti akampachike pa mtanda.

-Aloma akafuna kukwapula munthu, ankagwiritsa ntchito chikwapu chimene chinkakhala ndi chogwilira, ndipo kutsogolo kwa chogwiliracho, ankamangilira nthambo za zitsulo (mawaya), komanso kutsogolo kwa nthambozo, ankamangilira mafupa kapena miyala.

-Aloma akamakwapula munthu, ku nsana kwa munthuyo kunkadukaduka ndipo kaŵirikaŵiri munthuyo ankafa.

-Yesu atatha kukwapulidwa, asilikali anamunyoza Iye.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:16-20

16-Ndipo asilikali anachoka naye [Yesu] naloŵa naye m'bwalo, nalisonkhanitsa gulu lonse la asilikali.
17-Ndipo anamumveka Iye chibakuwa, naluka nkhata ya minga, namumveka Iye.
18-Ndipo anayamba kumulalatira Iye kuti, "Tamuwoneni mfumu ya Ayuda!"
19-Ndipo amamupanda Iye pa mutu ndi bango, namuthira malovu, namugwadira, namulambira.
20-Ndipo atatha kumunyoza, anamuvula chibakuwacho, namumveka Iye zovala zache.

-Asilikali anamumenya Yesu ndikumulavuliranso malovu.



34-Ndipo pa ora lachisano ndi chinayi, Yesu anafuwula ndi mawu okweza akuti, "Eloi, Eloi, lama sabakitani?" kutanthawuza kuti, "Mulungu wanga, Mulungu wanga , mwandisiyilanji Ine?"

-Pamene Mulungu Atate ankamusiya Yesu pa mtanda paja, Yesu analira.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu Atate anamusiya Yesu?

-Kodi Yesu anachimwako?
-Ayi.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu Atate anamusiya Yesu?
-Mulungu Atate ankapereka chilango kwa Iye chifukwa cha machimo anu, machimo anga, ndi machimo anthu onse.

-Chifukwa chakuti Mulungu Atate ankapereka chilango kwa Yesu chifukwa cha machimo athu, Iye anamusiya Yesu pa mtanda paja.

-Kodi Mulungu anati kuti chidzachitike ndi chiyani kwa Adamu ndi Hava akadzadya chipatso chimene Mulungu anaŵalamula kuti iwo asachidye m'munda wa Edeni muja?
-Adzafa.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anachimwa, iwo anafa chifukwa chakuti anali osiyanitsidwa kwa Mulungu.

-Tsopanonso, Yesu ankasiyanitsidwa kwa Mulungu Atate pa nthaŵi imeneyo..

aphunzitsi a malamulo anamutozanso mwa iwo okha. Ankati kuti, “Iye wapulumutsa anthu ena, koma sangathe kudzipulumutsa yekha!

32-Atsike tsopano pa mtandapo, Kirisitu, Mfumu ya a Isirayeli, kuti tiwone, ndikukhulupilira.”Ndiponso iwo amene anamupachika naye pamodziwo, anamulalatira.

-Yesu analankhula kuti ngati Ayuda awononge kachisi, Iye adzamanganso m’masiku atatu okha.

-Kodi Yesu ankakamba za kachisi wa miyala amene Ayuda anamanga mu Yerusalemu?
-Ayi.

-Kodi kachisi amene ankatanthawuza Yesu anali uti?
-Yesu ankatanthawuza thupi lache.

-Yesu ankatanthawuza kuti ngakhale kuti Ayuda amuwononge Iye pomupachika pa mtanda, adzawukanso pa masiku atatu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:33

33-Ndipo pofika ora lachisano ndi chimodzi, panali mdima pa dziko lonse, kufikira pa ora la chisano ndi chinayi.

-Kodi chifukwa chiyani kunali mdima pa dziko lonse kwa ma ora atatu?
-Ma ora atatuwo anali chizindikiro.

-Kodi chizindikiro chake chinali cha chiyani?
-Mulungu Atate ankamusiya Yesu pa mtanda paja.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:34



-Ngati m’mene Mulungu ananenera kudzera mwa aneneri mu zaka zambiri zapitazo, Yesu anayeneradi kumenyedwa ndi kulavulilidwa mate.

-Chifukwa chakuti anthu ankaŵalemekeza mafumu awo poŵagwadira , asilikali ankamunyoza Yesu pomugwadira.

-Chifukwa chakuti mafumu ankavala chisoti chapadera cha golide, asilikali anamunyoza Yesu pomumveka nkhata ya minga pa mutu pache.

-Ngati m’mene Mulungu ananenera kudzera mwa aneneri mu zaka zambiri zapitazo, Mpulumutsi ankayenera kunyozedwadi.

-Kodi nkhata ya mingayo inali chizindikiro cha chiyani?
-Nkhata ya mingayo inali chizindikiro cha thembelero la Mulungu.

-Adamu ndi Hava atachimwa, Mulungu analitembelera dziko la pansi ndipo anati kuti minga zidzimera.

-Asilikali aja atamumveka Yesu nkhata ya minga pa mutu pache, kodi chimenechi chinali chizindikiro cha chiyani?

-Chizindikiro chakuti Yesu ndi amene atenge thembelero la Mulungu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:21-22

21-Munthu wina wache wa ku Kurene, dzina lache Simoni, atate awo Alesandere ndi Rufu, ankadutsa kuchokera ku munda, anamukakamiza iye kuti anyamule mtanda wache.

22-Ndipo anamutenga [Yesu] ndikunka naye ku

malo otchedwa Gologota (kutanthawuza kuti Malo a bade)

-Asilikali anamutengera Yesu pa phiri lotchedwa Gologota, kunja kwa Yerusalemu, kukamupachika Iye.

-Pa phiripo, asilikali anayika mtanda pansi, kenako anamugoneka Yesu pamwamba pa ntandawo.

-Kenako anamukhomelera manja ake pamodzi ndi mapazi ache ndi misomali yayikuruyikuru.

-Ngati m'mene Mulungu ananenera kudzera mwa aneneri mu zaka zambiri zapitazo, manja ndi miyendo ya Mpulumutsi inayeneradi kuti abowoledwe.

-Asilikali aja atatha kumukhomelera Iye pa mtandapo, iwo anayimitsa mtandawo, Yesu ali chikhomeredwele pompo.

-Kodi mukukumbukira zimene Yesu anamuwuza Nikodemasi?

-Yesu anati kuti, ngati m'mene Mose anakolekera njoka ya mkuwa ija pa mtengo kuti anthu apulumutsidwe, chomchonso Yesu adzakolekedwa kuti anthu apulumutsidwe.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:23-24

23-Ndipo anamupatsa Iye vinyo osakaniza ndi mure, koma Iye sanamulandire.
24-Kenako anamupachika Iye, nagaŵanagaŵana zovala zache mwa iwo okha, pochita mayere pa izo, kuti adziŵe aliyense kuti atenga chiyani..



-Asilikali aja anamupatsa Yesu vinyo osakaniza ndi mure kuti achepetse ululu., koma Iye sanalandile.

-Asilikali amene anamukhomelera Yesu pa mtanda paja anapanga mawula pa zovala za Mpulumutsi.
-Ngati m'mene Mulungu ananenera kudzera mwa aneneri mu zaka zambiri zapitazo, iwo anapangadi mayere pa zovala za Mpulumutsi.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:25-27

25-Ndipo panali pa ola lachitatu pamene anamupachika Iye.
26-Ndipo lembo la mulandu wache linalembedwa pamwamba lakuti, MFUMU YA AYUDA.
27-Ndipo anaŵapachikanso achifwamba aŵiri pamodzi ndi Iye, wina kumanja wina kumanzere.

-Anthu enanso aŵiri anapachikidwa pamodzi ndi Yesu, wina ku manja, wina ku mamzere.

-Iwo anali anthu oyipa kwambiri.

-Ngati m'mene Mulungu ananenera kudzera mwa aneneri mu zaka zambiri zapitazo, Mpulumutsi anayeneradi kufa pamodzi ndi anthu oyipa kwambiri.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 15:29-32

29-Ndipo amene ankadutsapo ankamuchitira mwano Iye, namapukusa mitu yawo, namati, "Chomcho iwe opasula kachisi ndikumumanganso masiku atatu,
30-tsika pa mtandapo, ndipo uzipulumutse iwe mwini!"
31-Chimodzimodzinso akuluakulu a amsembe ndi